- Kenako ofuna thandizoyo ayenela kufotokoza tsatanetsatane wamapezedwe ake a ndalama papempho lovomelezekalo.
- Zimene ofuna thandizo wauza ogwira ntchito za malamulo, komanso zomwe walemba pa pempho lakelo ndi zipepala zina zonse zoikila umboni wa pempholi zimaperekedwa kwa wankulu oyendetsa za malamulo ndipo iye ndi amene amapeleka chiganizo kuti munthu ofuna thandizoli apatsidwe thandizo akupemphalo kapena ayi.
- Nkulu oyendetsa za malamulo ku ofesiyi amapanganso chiganizo cha gawo la ndalama limene ofuna thandizoyo adzayenela kupereka ku boma kuti alandire thandizolo.
- Pomaliza nkhaniyi imapekedwa kwa katswiri wa za zamalamulo amene ayiyendetse

## Kumene kuli ma ofesi athu

Padakali pano ofesi yathu ikupezeka ku malo anayi amene ali; likulu lathu ku Lilongwe mu nyumba ya Shire Building ndipo iyi imayang'anira chigawo chapakati.

Ku Blantyre ma ofesi athu ali ku ma ofesi a boma kumene kulinso maofesi a nthambi yoona anthu olowa ndi kutuluka mu dziko muno (Immigration) ndipo imayang'anira zochitika ku chigawo chakum'mwela.

Ku Mzuzu, maofesi athu ali mu nyumba ya Osman Gani ndipo imayang'anira kuchigawo chakumpoto.

Pomaliza ku Zomba, maofesi athu ali mu nyumba imene muli bwalo lalikulu la milandu momwe kale munali nyumba ya malamulo ndipo imayang'anira maboma a chigawo chakum'mawa.

# THE LEGAL AID BUREAU

*Chithandizo cha pamwamba pankhani za malamulo ku mtundu onse*

MALAWI LEGAL AID BUREAU

Quality legal aid services to the nation


### Head Office
1st Floor Shire Building
Off Paul Kagame Highway
P.O. Box 675
Lilongwe
Tel: + (265) 01 753 945 / Fax: + (265) 01 757 616

### Blantyre Office
Government Office Building
Lower Victoria Avenue
P.O. Box 569
Blantyre
Tel: + (265) 01 822 082 / Fax: + (265) 01 827 125

### Mzuzu Office
1st Floor Osman Gani Building
P.O. Box 282
Mzuzu
Tel: + (265) 01 311 086 / Fax: + (265) 01 312 505

### Zomba Office
Old Parliament Building
P.O. Box 362
Zomba
Tel: + (265) 01 528 856 / Fax: + (265) 01 528 860

***Email: info@legalaidbureau.org***
***Address all communication to the Director***



Republic of Malawi

European Union


# THE LEGAL AID BUREAU

*Chithandizo cha pamwamba pankhani za malamulo ku mtundu onse*


MALAWI LEGAL AID BUREAU

Quality legal aid services to the nation



SAMPLE
SAMPLE

# THE LEGAL AID BUREAU

MALAWI LEGAL AID BUREAU
Quality legal aid services to the nation

SAMPLE

## Chiyambi

Ofesi yothandiza anthu pankhani za malamulo ya Legal Aid Bureau inakhazikitsidwa potsatira gawo lachitatu la lamulo la Legal Aid Act la chaka cha 2011. Ofesiyi inakhazikitsidwa kuti idzipereka thandizo pankhani za malamulo kwa anthu amene sangakwanitse kulipira akatswiri a za malamulo oyima paokha. Ofesiyi ndiimodzi mwa ntchito zofunikila ku moyo wa tsiku ndi tsiku kwa anthu zomwe boma limapereka kwa anthu ake monga za umoyo, maphunziro, chakudya ndi madzi. Ofesi ya Legal Aid Bureauyi ndi yokhayo imene ili ndi ntchito yamtunduwu ku Malawi kuno.

## UDINDO

Ofesi ya Legal Aid Bureau imayesetsa mwakuthekela kwake kuchilimika pakupereka thandizo lokhazikika, thandizo losavuta kupeza, lotsata umunthu ndilapamwamba pankhani za malamulo, kwa anthu ovutika ku Malawi. Ofesiyi imaphunzitsanso anthu za malamulo.

## ZOLINGA

Ofesi ya Legal Aid Bureau ili ndi ntchito zikuluzikulu zimene zili:

- Kupereka malangizo pankhani za malamulo, kupereka thandizo pa nkhani za malamulo kuphatikizapo kuyimila anthu ovutika kumabwalo a milandu kapena mabwalo ena ofanana nawo.
- Kuphunzitsa anthu ndikuwapatsa zoyenela kudziwa pa nkhani za malamulo.

## NTCHITO ZA OFESI YOTHANDIZA ANTHU PA NKHANI ZA MALAMULO YA LEGAL AID BUREAU

Ofesi ya Legal Aid imagwira ntchito yayikulu poonetsetsa kuti anthu ochepekeledwa akupeza chilungamo ndi mayankho oyenela pa nkhani za malamulo monga momwe gawo 41 la malamulo akulu oyendetsera dziko lino limanenela. Ofesi ya Legal Aid imapereka thandizo kwa anthu amene alibe kuthekera kolipira akatswiri a malamulo oyima paokha. Thandizoli limaperekedwa kwa anthu ochepekeledwa kapena kuti omwe ali ovutika ndipo alibe kuthekera kupeza akatswiri owaimilira pa nkhani za malamulo oima paokha makamaka anthu omwe alibe kuthekerawa monga amayi, ana, achikulire, ndi odwala. Thandizo pa nkhani za malamulo liri m'magawo anayi:

(a) Thandizo kwa anthu amene akuganiziridwa kuti anaphwanya malamulo a dziko.
(b) Thandizo kwa anthu amene akuganiziridwa kuti anaphwanya malamulo okhudza munthu ndi munthu nzake.
(c) Malangizo ndi thandizo pa malamulo.
(d) Kuphunzitsa anthu momwe malamulo amayendela.

### *(a) Thandizo kwa anthu amene akuganiziridwa kuti anaphwanya malamulo a dziko*

Thandizoli limaperekedwa kwa anthu amene bwalo la milandu likuwazenga milandu yosiyanasiyana komanso kwa anthu amene akufufuzidwa pokayikiridwa kuti aphwanya malamulo adziko. Milanduyi ili monga ya kupha, kugwililira, kuba, ndi milandu ina iliyonse imene ingabwere chifukwa chakuphwanya malamulo ovomerezeka. Thandizoli liri monga malangizo pa za malamulo, kufunsa bwalo kuti limutulutse munthu pa belo, kapena thandizo lina lirilonse la malamulo.

### *(b) Thandizo kwa anthu amene akuganiziridwa kuti anaphwanya lamulo lokhudza munthu ndi munthu nzake*

Thandizoli limaperekedwa pamilandu yonse yokhudza munthu ndi munthu nzake kuphatikizapo nkhani za ana, mabanja, kutenga mwana amene sanaberekedwe ndi munthu kuti akhale ngati mwana wake, mikangano yokhudza malo, kufuna kupeza chipukuta misonzi pamene munthu wavulazidwa, kulakwira munthu nzake, chuma chamasiye ndi nkhani zokhudza malamulo a ntchito.

### *(c) Malangizo ndi chithandizo pa malamulo*

Ofesi ya Legal Aid imaperekanso malangizo ndi chithandizo pa nkhani za malamulo. Maphunzirowa amakhudza zinthu zosiyanasiyana monga za malamulo ndi ndondomeko zoyenela kutsata, momwe malamulo amayendera, thandizo pa pamalamulo pofuna kupewa kulipila chindapusa komanso malangizo ku bwalo la milandu.

### *(d) Kuphunzitsa anthu momwe malamulo amayendela*

Ofesi ya Legal Aid imaphunzitsanso anthu za momwe malamulo amayendela . Chidwi chachikulu chimayikidwanso pophunzitsa anthu za ofesi ya Legal Aidyi ndi ntchito zake.

## Ndondomeko

Kuti munthu athe kupeza thandizo ku ofesi ya Legal Aid ndondomeko izi zimayenela kutsatidwa:

- Akafika ku ofesi yathu, munthu ofuna thandizo kapena omuyimilira amakumana ndi ogwira ntchito za malamulo amene amamva dandaulo la munthu ofuna chithandizoyo.
- Ngati ofuna thandizoyo kapena oganiziridwayo sanabwere yekha chifukwa chakuti ali kundende, njira ina imakonzedwa mwamsanga kuti oganiziridwayo akafunsidwe mafunso kumalo amene akusungidwako ndicholinga chakuti opereka thandizoyo akamve zambiri.
- Ofuna thandizoyo ameyenela kulemba pempho lovomelezeka kuti athe kupeza thandizo.